# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

*Malangizo ndi Chilimbikitso kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino*


## FANO LALIKULU – UNENERI WA DANIELE WA UFUMU WA MULUNGU

"Ili ndi loto; kumasulira kwake tsono tikufotokozerani…" (Daniele 2:36). Danilele ananena choncho kwa Mfumu Nebukadinezara, amene amalamulira mwa mphamvu komanso molimba pa ufumu wonse wa Babiloni, umene unali ufumu waukulu kwambiri ndi wamphamvu mwa maufumu onse amene anakhala padziko. Mfumuyo inavutika ndi loto limene sinkatha kukumbukira. Kudzera mu mphamvu ya Mulungu, Daniele anaulula chinsinsi cha lotolo komanso kumasulira kwake.

Mfumuyo inalota chifano chachikulu cha munthu chitaima pambali pake. Mutu wake unali wa golide, manja ndi m'chifuwa mwake munali mwa siliva ndipo m'mimba mwake ndi m'tchafu mwake munali mwa mkuwa, miyendo yake nikhala yachitsulo ndipo pomaliza mapazi ake anali osakaniza chitsulo ndi dongo. Daniele anafotokoza kuti chifanocho chimaimira maufumu anai a pa dziko lonse amene adzabwere motsatanatsatana.

Mutu wa golide umaimira Nebukadinezara ndiponso ufumu wake wamphamvu wa Babiloni. Ufumu umenewu unali woyamba ndi waukulu kwambiri mwa maufumu onse a padziko lapansi amene anatuluka kuchokera mu ufumu wakale uja wa Asiriya umene unakhazikitsidwa ndi Nimurodi. Nebukadinezara analamulira pa ufumu wolemerawu kuyambira m'chaka cha 606 mpaka 561 B.C. (Yesu asanabwere).

Daniele adanenera za kugwa kwa ufumu wa Babiloni komanso kudzuka kwa ufumu waukulu wachiwiri. Uneneri umenewu unakwaniritsidwa m'chaka cha 538 B.C. pamene Mfumu Dariyo wa Amede ndiponso Kirusi Wamkuluyo mfumu ya




Aperesi anagwirana manja ndi kugonjetsa Ababiloni (Daniele 5:31). Izi zinapangitsa kuti padzuke ufumu wina wocheperako mphamvu wa Amede ndi Aperesi umene umaimira manja ndi m'chifuwa za siliva zija.

Mfumu Aleksandro Wotchukayo analanda ufumu wa Aperesi ndipo anagonjetsa dziko lonse la nthawi imeneyo m'chaka cha 330 B.C. Ufumu wa Agriki, umene ukuimira m'mimba ndi ntchafu za mkuwa, tsopano unakhazikitsidwa. Panthawi imene anamwalira Aleksandro Wotchukayo, ufumu wake unagawidwa panai pakati pa akulu ake ankhondo anai. Choncho ufumuwo unali wofooka mpaka pamapeto ake unagonjetsedwa ndi Aroma m'chaka cha 146 B.C.

Ufumu wa Aroma, unali ufumu womaliza wolamulira dziko lonse, ndipo ukuimira miyendo ya chitsulo. Mapazi, osakaniza chitsulo ndi dongo akuonetsa kuti ufumu wa Aroma udzakhala wosakhazikika ndipo mkati mwake mudzakhala kukangana ndipo izi zinachitikadi pamene ufumu wa Aroma unagawikana pakati pa maufumu ena ang'onoang'ono okwana 10. Palibenso mauneneri ena amene akuperekedwa a ufumu wina wa padziko lapansi wokhala ndi ulamuliro wamphamvu chotere.

Yesu Khristu anabadwa pa nthawi imene dziko lapansi linali pansi pa ulamuliro wa Aroma, amene mtsogoloeri wao anali Kaisara Augusto. Daniele ananenera kuti, "Ndipo masiku a mafumu aja Mulungu wa Kumwamba adzaika ufumu woti sudzaonongeka kunthawi zonse… nudzakhala chikhalire" (Daniele 2:44).

*(Yapitirira pa tsamba 1)*


Mau a Mkonzi — Tsamba 3
Kusanthula Baibulo-Za Ufumu wa Mulungu — Tsamba 4
Nkhani Yotsatana Nayo — Tsamba 5-6
Mauneneri a Ufumu wa Mulungu — Tsamba 7
Mafunso ndi Mayankho: Kodi Yesaya 11 akutanthauza chiyani? — Tsamba 8-9
Kodi Mukudziwa? Mau a pa Nyengo yake — Tsamba 10

# zimene BAIBULO limaphunzitsa za...

**Mau a Mulungu**
2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35
**Ubale wa Chikondi**
Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11
**Kulapa**
Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10
**Kubadwa mwatsopano**
Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4; Aef. 2:1, 5-6
**Kupulumuka ku uchimo**
1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11
**Chidzalo cha Mzimu Woyera**
Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8
**Chiyero**
Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16; Tit. 2:11-12; Aro. 6:22
**Ufumu wa Mulungu**
Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36
**Mpingo**
Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13; Akol. 1:18
**Umodzi**
Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4
**Maskaramenti**
Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30; 1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17
**Machiritso**
Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16
**Chiyero cha Banja**
Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3; 1 Akor. 7:10-11
**Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena**
1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5
**Masiku omaliza**
2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10; Mat. 25:31-46
**Kukhala mwa mtendere**
Luk. 6:27-29; Luk. 18:20
**Kupembedza**
Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17
**Kulalikira Uthenga Wabwino**
Mrk. 16:15

*(Kuchokera pa tsamba 1)*

Nebukadinezara analota mwala, wosemedwa kuchokera m'phiri koma wopanda manja, umene unaphwanya ndi kunyenya chifano chija. Kenaka mwalawo unadzasanduka chiphiri chachikulu ndipo chinadzaza dziko lonse. Umenewu ndi uneneri wa ufumu wodabwitsa wa Mulungu umene unakhazitsidwa m'masiku a mafumu amenewo.

Yesu ndiye mwala umene amisiri opanga nyumba anaukana koma unadzasanduka mwala wokhala pa ngondya (Machitidwe 4:11). Iye anabadwa mwa namwali ndipo ufumu wake unayamba pamene Yesu anabwera ngati mwana wolonjezedwa ndi Yesaya mneneri. "Pakuti kwa ife mwana wakhanda wabadwa….ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lake…Za kuenjezera ulamuliro wake, ndi za mtendere sizidzatha" (Yesaya 9:6-7).

Maufumu anai a dziko lonsewa anagwa mmodzimmodzi motsatizana, koma pali ufumu umene unadzuka pa nthawi imeneyo umene sudzagonjetsedwa. Umenewu ndi ufumu wa padziko lonse wa Yesu Khristu. Umenewu si ufumu wathupi koma wauzimu, ufumu wakumwamba umene sudzatha. Uthenga Wabwino wakhala ukulalikidwa padziko lonse. Maiko ayesetsa kufufuta chikhristu, komabe Ufumu wa Mulungu umanka upitirirabe kufalikira.

Anthu ambiri amadikira opanda chiyembekezo Ufumu wa Mulungu umene ulinkudza padziko lino. Ufumu wa Mulungu ulipo panopa pa nthawi ino. Unabwera poyamba ndi kubwera kwa Yesu koyamba kuja ndipo sitifunikanso kuti tiyembekezere nthawi ina. Lero ndi tsiku lako la chipulumutso ndipo ndi nthawi ino ndi imene tingalowemo mu mtendere, bata ndi zokoma zosiyanasiyana zimene zimaperekedwa ndi ufumuwo.

-mws

## UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

## KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu ililyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa *email*, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma *email* a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

## KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.us

# Mau a Mkonzi



*"Musaopa, kagulu ka nkhosa inu; chifukwa Atate wanu akonda kukupatsani Ufumu"* (Luka 12:32).

Ndinali ndi mtima wa chiyamiko pamene ndimalemba kalata uyu wa *Uthenga wa Choonadi*. Kwa miyezi ingapo yapitayi, ndadutsa mu zokhoma ndi zopsinja pa moyo wanga. Ndipo pano ndikadali m'chigwa cha zopsinjachi. Mulungu wandipatsa mphamvu ndi kulimba mtima kuti ndikhoza kulemba kalatayu – imene sindikanakwanitsa kulemba mwezi wathawu. Mzonse, Ambuye wakhala nane ngakhale mnyengo za mdima pa moyo wanga. Panali nthawi zambiri zimene ndinanena kuti, "Zikomo Yesu, chifukwa chokhala bwenzi langa." Mulungu watsimikiza chikondi chake ndi mphamvu yake kangapokangapo.

Winawake adandiuzapo kuti tikhoza kuzunzika limodzi ndi Ambuye kapena tikhoza kuzunzika popanda Iye. Ndikuyamika Mulungu chifukwa cha mwayi wozunzika pamodzi ndi Mpulumutsiyo. Pamene ndimadutsa m'mayesero ndi m'namondwe pa moyo wanga, panalibe chitetezo china chachikulu koposa mu mnthunzi umene upezeka dzanja la Mulungu. Kuvutika ndi matenda a mtima komanso zowawa zina zimabwera m'moyo uno, koma kupezeka kwa Mulungu kumatipatsa mphamvu ndi kulimbika kuti tifikenso tsiku lina. Ndikhoza kulankhula ngati Yobu kuti, "Mombolo wanga ali ndi moyo." Pa minga iliyonse ndi mthenga wa Satana amene amandisautsa, pakhala madalitso ochuluka ndi angelo a kuunika amene anaima pambali yanga nandithandiza ndi kundionetsera chikondi. Tili ndi mwai waukulu kuti tili m'banja la Mulungu. Pamene mmodzi azunzika, tonsefe timazunzika naye limodzi. Ndikuthokoza kwambiri aliyense wa inu amene mwakhala mukuima nane komanso mukupitiriza kuima nane pamodzi ndi banja langa m'mapemphero. Mapempherowa sanapite pambali ayi.

Ine ndili odalitsika kwambiri kukhala mbadwa ya Ufumu wa Mulungu. Ndanenapo zina mwa zinthu zimene zokhudza ufumu wodabwitsawu mu kalata ino. Ndilibe malo okwanira akuti ndinganene za kukongola kochititsa kaso komanso choonadi chenicheni cha ufumuwu. Pemphero langa ndilo lakuti Mzimu Woyera atenga zimene talemba m'kalatayi ndi kuzichulukitsa kwa mzimu wa iye amene akuwerenga. Anthu ambiri akufuna kuti Khristu akhazikitse Ufumu wake pansi pano kuti padzakhale mtendere komanso chuma ndi katundu wochuluka. Ineyo ndikuwuona ufumuwo ukugwira ntchito pamoyo wanga panopa. Pamene munthu wakunja akuonongeka, munthu wamkatiyo akukonzeka tsiku ndi tsiku. Ine ndili gawo la ufumu wauzimu umene sungaonongeke. Namondwe akhoza kuomba, koma makomo a gehena sangathe kugonjetsa Ufumu wa Mulungu. Sindingalole kusinthitsa zokoma zimene zipezeka pokhala mbadwa ya Ufumuwo ndi chuma kapena ulemerero wonse wa dziko lino lapansi.

Tiyeni tikhale oona ndi okhulupirika kwa Ambuye wathu ndi Mfumu yathu. Mwa Iye, muli mtendere umene umapambana chidziwitso chonse. Pamene ndikusangalala ndi madalitso a mu ufumuwu, ndikuyang'anira ndi chiyembekezo Ufumu wa Kumwamba umene udzakhala ku nthawi zamuyaya.

Michael W. Smith

April 2013

Zambiri Zili pa

INTANETI

*Mukafuna kutipeza pa intaneti, mulembe www.thegospeltruth.us kuti mudzilandira makalata athu kapenanso kuti muone makalata akale.*



**Kodi Zili ndi Kanthu?**

"Ukhulupirire zimene ukufuna, inenso ndikhulupirira zimene ndikufuna. Tonsefe tikupita ku malo amodzi omwewo, ndipo chiphunzitso cha mpingo wathu chilibe kanthu". Mkhristu wolemekeza mipingo yonse amatero.

Kumeneku ndi kuganiza kolakwika popeza pali choonadi chimene Baibulo limanena posawerengera zimene mipingo imaphunzitsa kapena kukhulupirira.

Chiphunzitso choona cha Ufumu wa Mulungu monga ufumu wa uzimu nchofunikira. Anthu akadziwa zoona zenizeni, anthuwo akhoza kufunafuna choonadicho m'moyo wawo walero kusiyana ndi kuyembekezera zina zakutsogolo zimene mwina sizidzabwera.

Palibe mwayi wina wakuti anthu ochimwa apulumutsidwe. Sipadzakhala mwayi wachiwiri kutsogoloko kuti anthu apange ubale ndi Mulungu. Lero ndilo tsiku la chipulumutso."

Choncho,

**ZILI NDI KANTHU**

# KALOZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

## Mutu: Za Ufumu wa Mulungu

**Mau a Mulungu:** *Luka 1:31-33 Ndipo taona, udzakhala ndi pakati, nudzabala mwana wamwamuna, nudzamutcha dzina lake Yesu. Iye adzakhala wamkulu, nadzatchedwa Mwana wa Wamkulukulu: ndipo Ambuye Mulungu adzampatsa Iye mpando wachifumu wa Davide atate wake: ndipo Iye adzachita ufumu pa banja la Yakobo kunthawi zonse; ndipo ufumu wake sudzatha.*

**Kuomba mkota:** *Ufumu wa Mulungu si ufumu wa dziko lino umene udzakhazikitsidwe mtsogolo muno, koma ndi ufumu wauzimu umene wakhazikika m'mitima yathu kudzera mwa Yesu Khristu.*

**1. Malo ake a Ufumuwo**
- A. Yohane 18:36-37 Si wa dziko lino ayi.
- B. Luka 17:20-21 Uli mkati mwanu.

**2. Ufumuwo ndi wauzimu**
- A. Aroma 14:17 Chilungamo, mtendere ndi chimwemwe.
- B. 1 Akorinto 4:20 Ufumuwo uli mu mphamvu.

**3. Nthawi imene udzakhazikitsidwe**
- A. Luke 16:16 Kulalikira za ufumuwo kunayamba nthawi ya Yohane Mbatizi.
- B. Luke 4:43 Yesu analalikira za ufumuwo.
- C. Marko 1:14-15 Nthawi yakwana, ndipo ufumu wa Mulungu wayandikira.
- D. Marko 9:1 Unalonjezedwa kwa ophunzira asanamwalire.
- E. Machitidwe 1:1-3 Lonjezano linakwaniritsidwa ndi Mzimu Woyera.

**4. Kulowa mu Ufumuwo**
- A. Yohane 3:3 Muyenera kubadwanso mwatsopano.
- B. Luka 16:16 Ukangamireni.

**5. Kulamulira mu Ufumuwo**
- A. Chivumbulutso 1:5-6 Iye watipanga ife kukhala mafumu ndi ansembe.
- B. 1 Petro 2:9-10 Mbadwa zosankhika, mtundu woyera mtima.
- C. Aroma 6:14-15 Mphamvu pa uchimo.
- D. 1 Yohane 5:4 Mphamvu pa dziko lapansi.
- E. Chivumbulutso 15:2-3 Chigonjetso pa chipembedzo chonyenga.
- F. Luka 10:17-20 Mphamvu pa Satana.

**6. Chitsimikizo chakuti Ufumuwo waikika kale**
- A. Ahebri 12:28 Tinalandira ufumu.
- B. Akolose 1:12-13 Watisanduliza kuti tilowe mu ufumuwo.
- C. Chivumbulutso 1:9 Yohane naye ali mu ufumuwo.

**7. Nthawi imene Ufumuwo udzakhalepo**
- A. Yesaya 9:6-7 Udzakhazikika mpaka kalekale.
- B. Daniele 2:44 Sudzaonongeka

**Mau Omaliza**

*Luka 12:31-32 Komatu tafunafunani Ufumu wake, ndipo izi adzakuonjezerani. Musaopa, kagulu ka nkhosa inu; chifukwa Atate wanu akonda kukupatsani Ufumu.*

## AYUDA AMAFUNA KUOMBOLEDWA KU CHIPSINJO CHA ULAMULIRO WA MASIKU AMENEWO

Anthu Achiyuda anali pansi pa ulamuliro wa boma la Aroma, ndipo amafunafuna Mesiya woti akhoza kubwera ndi kudzaombola dziko lao ku ulamulirowu ndipo kenaka Mesiyayo akhazikitse Ufumu wake. Iwo amawerenga zimene analosera aneneri akale kuti idzafika nthawi pamene Mwana wa Mulungu adzalamulire ndi mphamvu ndipo padzakhala mtendere, machiritso, ndi mamasulidwe. Ophunzira asanalandire Mzimu Woyera, iwonso anamufunsa Khristu kuti, "Ambuye, kodi nthawi yino mubwezera ufumu kwa Israyeli?" (Machitidwe 1:6). Ayuda, pokhala anthu, anamukana Khristu monga Mwana wa Mulungu chifukwa ufumu wao wa dziko lino unali usanabwezeretsedwe. Iwo komanso Akhristu ambiri akudikira nthawi ya mtsogolo imene Mesiya adzabwere ndi kukhazikitsa ufumu wake pansi pano. Zachisoni kuti tsiku limenelo silidzabwera. Mau a Mulungu amatiphunzitsa mwachimvekere kuti Ufumu wa Mulungu unakhazikitsidwa ndi kubwera koyamba kwa Yesu Khristu. Anthu amene akudikira tsiku lina la mtsogolo kuti Iye adzabwera ndi kukhazikitsa ufumu wake akungomanidwa zokoma ndi chimwemwe cha Ufumu wa Mulungu zimene zilipo lero komanso tsopano lino.



**"Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani Uthenga Wabwino."**
**Marko 1:15**

## UFUMU WA MULUNGU SI WATHUPI AYI

Yesu amadziwa kuti ufumu wake si wa Dziko lino ayi. Choncho, asanakhomedwe pamtanda ananena momveka bwino kwa ophunzira. Anati kwa Pilato, "Ufumu wanga suli wa dziko lino lapansi; ufumu wanga ukadakhala wa dziko lino lapansi, anyamata anga akadalimbika nkhondo…" (Yohane 18:36). Lemba lokhali likutsutsiratu zakuti Ufumu wa Mulungu ndi ufumu wa dziko lapansi. Afarisi anafuna kudziwa kuchokera kwa Yesu za tsiku nthawi imene udzabwere Ufumu wa Mulungu. Yesu anawayankha kuti, "Ufumu wa Mulungu sukudza ndi maonekedwe;…Pakuti, taonani, Ufumu wa Mulungu uli m'kati mwa inu" (Luka 17:20-21). Ufumu wa Mulungu si ufumu wa boma la pansi pano wokhala ndi likulu lake komanso mfumu yake pansi pano.

## UFUMUWO NDI WAUZIMU

Ufumu wa Mulungu ndi ufumu wauzimu mkati mwa mtima wa mwana wa Mulungu aliyense. Ndi chilungamo, Chimwemwe ndi mtendere zogwira ntchito m'moyo wa okhulupirira (Aroma 14:17). Mtendere weniweni sukhazikika pa zinthu zimene zili kunja kapena pa ma boma athu. Mtendere umabwera chifukwa cha zimene Mulungu wachita mumtima mwathu. Yesu anati, "Mtendere ndikusiyirani inu, mtendere wanga ndikupatsani; Ine sindikupatsani inu monga dziko lapansi lipatsa…" (Yohane 14:27).

## UFUMU UNAKHAZIKITSIDWA NDI YESU

Yohane Mbatizi anayamba kulalikira uthenga wa ufumuwo nawadandaulira anthu kuti atembenuke mtima. "Chilamulo ndi aneneri analipo kufikira pa Yohane; kuyambira pamenepo ulalikidwa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu, ndipo munthu aliyense akangamira kulowamo" (Luka 16:16). Yesu anaphunzitsa momveka bwino kuti, "Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino." (Marko 1:15). Ufumuwo sunali kubwera mtsogolomu koma unali utakhazikitsidwa kale mwa Khristu. "Koma Ine ndinena ndi inu zoonadi, Kuli ena a iwo akuimirira pano, amene sadzalawatu imfa, kufikira kuti adzaona Ufumu wa Mulungu. " (Luka 9:27)

## KODI MU UFUMUWO TIMALOWAMO BWANJI?

Yesu anauza Nikodemo kuti, "Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu" (Yohane 3:3). Munthu amalowa mu ufumuwu pamene walapa machimo ake ndipo walola Yesu kukhala mfumu ya moyo wake. Mphamvu ya ufumuwo inaperekedwa pa tsiku la Pentekoste pamene Mzimu Woyera anadzaza mitima ya ophunzira aja (Machitidwe 2). Chidzalo cha ufumuwo kudzera mwa mphatso ya Mzimu Woyera amene amapereka mphamvu, mtendere, chimwemwe, utsogoleri ndi chiyero.

*(Yapitirira pa tsamba 6)*

(Kuchokera pa tsamba 5)

### KULAMULIRA MU UFUMUWO

Yesu "...natiyesa ife ufumu tikhale ansembe a Mulungu ndiye Atate wache;..." (Chivumbulutso 1:6). Akhristu a mu ufumu wauzimuwu akhala ndi ulamuliro pa tchimo, pa iwo eni,pa dziko ndi pa chipembedzo chonyenga. Lero Khristu ndi mfumu yamphamvu zonse, ndipo amalamulira pa mpingo wake (Akolose 1:18) ndipo amalemba malamulo ake pa mitima ya anthu okhulupirira. Yesu amawaombola, kuwachiritsa ndi kuwayeretsa.

### ALIYENSE AKHOZA KULOWAMO

Ufumuwo wakhazikitsidwa ndipo wina aliyense angathe kuupeza kudzera mwa Yesu Khristu. "Mwa ichi polandira ufumu wosagwedezeka, tikhale nacho chisomo, chimene tikatumikire nacho Mulungu momkondweretsa, ndi kumchitira ulemu ndi mantha" (Ahebri 12:28). Ufumu umenewu unaloseredwa mwa uneneri ndipo unakwaniritsidwa ndi kubwera koyamba kwa Yesu Khristu. Ufumu umenewu sudzatha komatu udzakhalapo mpaka Muyaya (Yesaya 9:6-7).

ONANI: *Pamene Yesu adzabweranso kachiwiri, Iye adzabwera kudzatenga anthu ake ndi kuwalowetsa ku mpando wa Mulungu wa chiweruziro. Dziko limene timalionali lidzaonongedwa (2 Petro 3:10-12). Olungama adzalowa nawo kumwamba pamene wochimwa adzakhala nthawi zonse ku gehena Izi tidzaziona mu kalata ya Gospel Truth imene ikubwera.*



-mws

# Zofunikira Pofuna Kukhazikitsa ndi Kubweretsa Ufumu

*Zolemba za H.M. Riggle, (1902) mwachidule*



**1. MFUMU NGATI MUTU WOLAMULIRA.**

Matthew 21:4-5 Taona, Mfumu yako idza kwa iwe,

Akolose 1:18 Ndipo Iye ali mutu wa thupi, Eklesiayo; ndiye chiyambi, wobadwa woyamba woturuka mwa akufa; kuti akakhale Iye mwa zonse woyambayamba.

**2. MPANDO WACHIFUMU KUCHOKERA PAMENE MFUMUYO IMAPEREKA MALAMULO.**

Ahebri 1:8 Koma ponena za Mwana, ati, Mpando wachifumu wanu, Mulungu, ufikira nthawi za nthawi; Ndipo ndodo yachifumu yoongoka ndiyo ndodo ya ufumu wanu.

Ahebri 4:16 Potero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo,

**3. MALIRE AKE A MALO AMENE MFUMUYO IKHOZA KULAMULIRA.**

Mateyu 28:18 Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi.

**4. ADZALAMULIRA PA NZIKA ZA UFUMUWO.**

Yakobo 4:7 Potero mverani Mulungu;


1 Peter 3:22 amene akhala pa dzanja lamanja la Mulungu, atalowa m'Mwamba; pali angelo, ndi maulamuliro, ndi zimphamvu, zomgonjera.

**5. LAMULO LOGWIRA NTCHITO PA NZIKA ZA UFUMUWO.**

Ahebri 8:10 … Ndidzapatsa malamulo anga kuwalonga m'nzeru zao, Ndipo pamtima pao ndidzawalemba iwo; Ndipo ndidzawakhalira iwo Mulungu, Ndipo iwo adzandikhalira Ine anthu:

**MAU OMALIZA**

*Zinthu zonse zofunikazi zikupezeka komanso zikugwira ntchito mu nyengo ya chisomo. Yesu Khristu ndiye mfumu ya Kumwamba ndi Dziko lapansi ndipo amakhala ndi anthu ake. Iye amakhala pa mpando wachifumu ndipo ndiye mutu wake wa mpingo. Lamulo lake la chiyero lili m'mitima ya oyera mtima onse ndipo iwo akulamulira m'moyo uno. Chifukwa cha ichi Ufumu wa Mulungu wakhazikitsidwa kale.*




| Uneneri | Kukwaniritsida |
|---|---|
| Yesaya 2:2-4 Nyumba ya Ambuye idzakhazikika. (Mika 4:1-7) | Ahebri 12:22-23 Inu mwafika ku Phiri la Ziyoni. |
| Salmo 2:6-9 Ufuma wa Mwana. | Machitidwe 13:33 Yesu wakwezedwa. |
| Salmo 110:1-3 Ambuye alamulira kuchokera mu Ziyoni. | Machitidwe 2:30,32-36 Yesu wakhala pa mpando washifumu. |
| Daniele 7:14 Ufumu wa ulamuliro ndi ulemerero. | Aefeso 1:20-22 Khristu ali ndi ulamuliro wonse ndi mphamvu zonse. |
| Yesaya 35:5-6 Matenda ndi madwale achiritsidwa. | Mateyu 4:23-24; 8:16-17 Yesu anachiritsa matenda onse. |
| Yesaya 35:6-7 Madera ouma adzasandulika. | Yohane 4:14 Yesu amapereka madzi opatsa moyo.<br>Yohane 6:35 Sadzamvanso njala kapena ludzu. |
| Mika 4:3-4 Mtendere wosaneneka. | Yohane 14:27 Yesu amapereka mtendere. |



*Komatu mwayandikira*
*Kuphiri la Ziyoni,*
*Ndi mudzi*
*Wa Mulungu wamoyo.*

# Mafunso ndi Mayankho

**Funso: Kodi Malemba atanthauzanji pa Yesaya 11 pamene akunena kuti nyama zakuthengo zidzakhalira pamodzi mu mtendere?**

**Yankho:** Tiyeni tiganizire za ndime imene funso limeneli likuchokerapo. "Mmbulu udzakhala pamodzi ndi mwanawankhosa, ndipo nyalugwe adzagona pansi ndi mwanawambuzi; ndipo mwanawang'ombe ndi mwana wa mkango ndi choweta chonenepa pamodzi; ndipo mwana wamng'ono adzazitsogolera. Ndipo ng'ombe yaikazi ndi chilombo zidzadya pamodzi; ndipo ana ao ang'ono adzagona pansi; ndipo mkango udzadya udzu ngati ng'ombe. Ndipo mwana wakuyamwa adzasewera pa una wa mamba, ndi mwana woleka kuyamwa adzaika dzanja lake m'funkha la mphiri" (Yesaya 11:6-8).

Limeneli ndi funso lufunikira ndi lomveka popeza pali zithunzi zambiri zimene zikuonetsa za mkango utagona pansi pamodzi ndi mwanawankhosa kusonyeza ulamuliro wa zaka 1,000 pansi pano pamene Khristu adzakhale atakhazikitsa Ufumu wake. Limenelo ndi bodza komanso kutanthauzira kolakwika kwa Malemba amene akupezeka pa Yesaya 11. Anthu akhala akulota ndi kungofanizira kuti kudzabwera nthawi imene kudzakhale mtendere pa dziko lonse komanso kopanda chiwawa ndi chipolowe ngakhale pakati pa zinyama. Anthu akhala akujambula zithunzi zochuluka zooneka bwino ndi mau okometsera pofuna kusonyeza za nthawi imeneyi imene ya ulemerero wa pansi pano.

Yesu anaphunzitsa kuti Ufumu wa Mulungu unali ufumu wa uzimu, osati wa dziko lapansi ayi. Yesaya 11 ndi uneneri wokongola ndi wofotokoza mwatsatsanetsane za mtendere wosaneneka ndi Chimwemwe zimene zimadza pamene munthu walandira chipulumutso kuchokera kwa Yesu Khristu. Sitiyeneranso kuyang'ana za kutsogolo kuti tipeze za kukwaniritsidwa kwa uneneri umenewu, popeza unakwaniritsidwa kale pa kubwera koyamba kuja kwa Mesiya.



**"Nyama zimene zikunenedwa si zinyama zenizeni monga timazidziwira, koma akukamba za anthu nawafanizira ndi chikhalidwe cha nyama."**

Tiyeni tioneko za mavesi ena amene akupezeka pafupi ndi ndimeyi kuti uneneriwu tiwumvetse bwino. "Ndipo padzatuluka mphukira pa tsinde la Jese, ndi nthambi yotuluka m'mizu yake idzabala zipatso" (Yesaya 11:1). Ndime iyi komanso Malemba amene ali kutsogolo kwake zikunena za Khristu Mwini amene anali chidzukulu cha Jese, amene anali atate ake a Mfumu Davide. "Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti muzu wa Jese umene uima ngati mbendera ya mitundu ya anthu, amitundu adzafunafuna uwu; ndipo popuma pake padzakhala ulemerero" (Yesaya 11:10).

Izinso zikunenedwa za Yesu mu Yeremiya 23:5 ndi mu Chivumbulutso 5:5 pamene akunena kuti, "Mkango wochokera m'fuko la Yuda, Muzu wa Davide, walakikika…"

Mtumwi Paulo akunena za pa Yesaya 11 ndipo akuwunikira kwa wowerenga za kukwaniritsidwa kwa uneneriwu mwa Khristu. "Ndipo ndinena kuti Khristu anakhala mtumiki wa mdulidwe, chifukwa cha choonadi cha Mulungu, kuti alimbikitse malonjezo opatsidwa kwa makolo, ndi kuti anthu a mitundu yina akalemekeze Mulungu, chifukwa cha chifundo; monga kwalembedwa, Chifukwa cha ichi ndidzakuvomerezani Inu pakati pa anthu amitundu, ndidzaimbira dzina lanu. Ndiponso anena, Kondwani, amitundu inu, pamodzi ndi anthu ake. Ndiponso, Tamandani Ambuye, inu a mitundu yonse; ndipo anthu onse amtamande. Ndiponso,

Yesaya ati, Padzali muzu wa Jese, ndi Iye amene aukira kuchita ufumu pa anthu amitundu; Iyeyo anthu amitundu adzamuyembekezera. Ndipo Mulungu wa chiyembekezo adzaze inu ndi chimwemwe chonse ndi mtendere m'kukhulupirira, kuti mukachuluke ndi chiyembekezo, mu mphamvu ya Mzimu Woyera" (Aroma 15:8-13).

Paulo amalangiza ampingo wa ku Roma kuti awalandire akhristu anzawo amene sali Ayuda komabe analowa mu Ufumu wa Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera. Khristu anakwezedwa pamtanda ndipo kudzera mu imfa ndi kuukitsidwa kwake, anthu onse ali ndi mwayi wolandira nawo cholowa cha mu Ufumuwo. Yesu samalamulira akhristu Achiyuda okha ayi koma akulamuliranso mu mitima ya akhristu amene sali Ayuda. "Anadza kwa zake za Iye yekha, ndipo ake a mwini yekha sanamlandire Iye. Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lake" (Yohane 1:11-12).

Mpumulo wa ulemerero umene ukunenedwa pa Yesaya 11:10 unaonetsedwa kwa okhulupirira pa nthawi ya Khristu. Uthenga wa Mesiya unali wakuti, "Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi kuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu." (Mateyu 11:28). Mpumulo ndi mtendere wodabwitsawu umene unanenedwa kale ukulozera ku mtendere umene Yesu anabweretsa kudziko lapansi. Chifukwa chake nzosadabwitsa kuti pa nthawi ya kubadwa kwa Mesiya angelo anaimba kuti, "Ulemerero ukhale kwa Mulungu Kumwambamwamba, ndi mtendere pansi pano mwa anthu amene akondwera nao" (Luka 2:14).

Titayikhazika ndimeyi pamalo ake oyenera, tikhozano kuyamba kutanthauzira ndimeyi moyenera. Tsopano tikudziwa kuti sitiyang'ana za kutsogolo koma zakumbuyo ndi zatsopano kuti tidziwe tanthauzo lake lakuti nyama zakuthengo zikhalire limodzi mwamtendere. Nzachidziwikire kuti zoterezi sizinachitikepo pakati pa zinyama nkale lomwe. Tiyeni tikumbukire kuti Ufumu wa Mulungu ndi wauzimu ndipo mpumulo komanso mtendere unalipo ndipo ulipobe lero lino pakati pa ana enieni a Mulungu. Choncho tiyenera kuyimvetsetsa ndimeyi mwauzimu. Uneneri uliwonse umaperekedwa mwazifanifani ndipo ndi mmene zikuchitikira apa pa Yesaya 11. Nyama zimene zikunenedwa apa sinyama zenizeni zakuthengo koma akunena za makhalidwe aunyama amene anthu ali nawo. Umu ndi mmene zimakhalira zinthu m'Chipangano Chakale ngakhalenso Chatsopano.



---

**Yesaya 11:6-8 akunena za nkhani ya nyama zimene mwachilengedwe zili zodana koma zikukhala pamodzi mwamtendere ... zofooka ndi zamphamvu... zonse zikukhalira pamodzi mosavuta**

---

Mneneri Ezekiele anati, "Akalonga ake m'kati mwake akunga mimbulu yakumwetula nyama, kukhetsa mwazi..." (Ezekiele 22:27). Yesu anauza ophunzira ake kuti, "Mukani; taonani, Ine nditumа inu ngati ana a nkhosa pakati pa mimbulu" (Luka 10:3). Yesunso ponena za Herode anati, "Pitani kauzeni nkhandweyo..." (Luka 13:32). Anthu amene akutchulidwawa anali ndi makhalidwe ofanana ndi a nyama zimene akuzinenazi. Mimbulu imaimira anthu amene amakonda kuipitsa ndi kuwononga anzawo. Nkhosa zikuimira mtima wa kudzichepetsa ndi kufatsa. Nkhandwe ingathe kuimira munthu amene ali kapsala.

Choncho pa Yesaya 11:6-8 akunena za anthu amene anali pa udani akukhalira limodzi mwa mtendere. Izi zikuimira nthawi ya bata pakati pa anthu ochokera kosiyana, ndi a makhalidwe osiyanasiyana. Anthu amene mwachibadwidwe ali osowa chitetezo amakhalira limodzi mwa mtendere ndi anthu amene mwachibadwidwe ali amphamvu ndi okadzula anzawo. Ofooka ndi amphamvu, zakuthengo komanso zowetedwa, oopsa ndi osaopsa onse akukhalira limodzi mwa bata. Kodi izi zingatheke bwanji? Izi ndi zotheka komanso ndiye zoonadi zenizeni za Ufumu wa Mulungu. Anthu a mitundu yonse ndi a makhalidwe onse amalowa mu ufumuwo kudzera mwa Yesu Khristu. Chikhalidwe chawo chakale chimasinthika ndipo zonse zakale zimasanduka zatsopano (2 Akorinto 5:17).

Anthu a Mulungu lero, amene ali pansi pa ufumu ndi ulamuliro wa Mesiya ali otetezeka ndi oyanjana. Iwo ndi olandira nawo moyo wa umulungu (2 Petro 1:4) ndipo makonda athu okana Mulungu, auchigawenga ndi achithupithupi amasinthidwa ndi kukhala a chikondi ndi a mtendere. Ndi chinthutu chodabwitsa kukhala mu Ufumuwo lero. Pa Yesaya 11:6-8 akutionetsa popereka chithunzi cha ufumu wokongola wa Mulungu umene ukulamulira lero.

Pamene tikusangalala ndi madalitso amenewa a ufumu wa uzimu wa mtendere umene uli m'moyo uno kudzera mwa Yesu Khristu, tiyenera kuyang'ananso ndi chiyembekezo chachikulu ku nthawi imene tidzakhale Kumwamba pamaso penipeni pa Mulungu mwini.

-mws

KODI **MUKUDZIWA?**

**Malemba:** "…ana amuna a Mulungu anayang'ana ana akazi a anthu…ndipo anadzitengera okha akazi onse amene anawasankha." Genesis 6:2

**Nthawi yake:** Mulungu asanaononge dziko lapansi pa nthawi ya Nowa.

**Ana amuna a Mulungu:** Zidzukulu za Seti ndi ena amene adapitirira kuopa Mulungu ndi kupembedza Mulungu ndipo anali ndi chikhalidwe choongoka.



**Ana akazi a anthu:** Awa ndi zidzukulu za Kaini ndi ena amene adasiya Mulungu natsata njira monga mmene thupi lawo linawalamulira.

**Malemba:** Wokhulupirira akakwatira ndi munthu wosakhulupirira uzimu wake umasungunuka ndi kuzimirira.

**Mau a pa Nyengo Yake**

# Pokhala ine Mumdima

*"…Pokhala ine mumdima Yehova adzakhala kuunika kwanga."* Mika 7:8

Pamene moyowu ukudutsa mnyengo za mdima, Ambuye adzabwera ndi kuphwanya mdima ndi kuunika kwa chikondi ndi choonadi chake. M'masiku tikumva ululu wa mthupi, kusautsika mmaganizo ndi kuvutidwa mumtima, Mulungu adzatizinga ndi kupezeka kwake, ndipo tidzakhala ndi chitetezo komanso chidziwitso cha kukhudzidwa kwake ndiponso chikhalidwe chake cha kuchiritsa.

Nthawi idzafika pamene mudzapezeka kuti mwakhala mu mdima pa moyo wanu – osasuntha nkomwe kapena kupita kutsogolo. Ngakhale tsogolo likuoneka kuti silikusonya kanthu ndipo zimene zikubwera sizikudziwika bwinobwino, timapeza mtendere pakupumula mu kuunika kwa Ambuye. Ndipo ndi m'kuunika kwakeko kumene timapeza kulimbika ndi mphamvu kuti tifika tsiku lina. Ambuye amakhumba atabwera ndi kudzakhala nanu ndi kubweretsa kuwala kwake kudzera mchivomerezo chake ndi chikondi chake chosatha pa inu. Dzikoli lili mu mumdima ndipo lipitirira kukhala choncho, koma choonadi chosatha cha Mau a Mulungu chimabweretsa kuwala kumene kumene kumationetsa njira yoti tiyendemo paofuna kutuluka mu mdimawo.



Ngakhale dziko lioneke ngati zinthu sizidzayenda ndipo ngakhale nyengo za pa moyo wanu zioneke ngati zada, Yesu anafika ku dziko lino kudzabweretsa chiyembekezo pamene panalibe chiyembekezo. Sitiyenera kukhala mu mdima kwa nthawi yaitali, popeza Bwenzi Lathu ndi Mpulumutsi wathu adzafika ndi kubweretsa kuwala komanso chimwemwe m'mitima yathu.

-mws

**KUTI MUTIPEZE**

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.us

CHIYERO CHA KWA AMBUYE